# Ayamikira pulojekiti ya ulimi wothirira

WOLEMBA:
ESMIE KOMWA

Wachiwiri kwa mtsogoleri wa dziko lino Saulos Chilima wayamikira mmene ntchito ya ulimi wothirira ya Shire Valley Transformation Programme (SVTP) ikuyendera.

Chilima adanena izi Lolemba pamene amakayendera ntchitoyi m'boma la Chikwawa.

Iye adati ntchitoyi yayamba bwino ndipo ikuyenda bwino chifukwa palibe chovuta chilichonse chimene wapeza atayendera. Iye adati choncho pakufunika kuwapatsabe nthawi ogwira ntchitoyi kuti aigwire mwaukadaulo ndi molimba.

"Ndaona kuti malo opatutsira madzi kuchokera mumtsinje wa Shire akukonzedwa ndipo ngalande yaikulu yotengera madzi pafupifupi makilomita 6 ikukonzedwa zimene zikusonyeza kuti ntchitoyi ikuyenda ndithu," adatero Chilima.

Iye adati pulojekitiyi ndi yaikulu kwambiri ndipo ikamalizidwa ndi kuyamba kugwiritsidwa ntchito moyenera isintha dera la kuchigwa cha mtsinje wa Shire chokha koma dziko lonse lino.

Kupatula kuthandiza kuti dziko lino lizidzidalira pa chakudya, Chilima adati pulojekitiyi ibweretsa ntchito za mafakitale m'dziko muno makamaka zokonza mbewu ndi kumagulitsa kumaiko akunja komanso isintha alimi ang'onoang'ono kukhala akuluakulu ndi kumalima mwa bizinesi.

Zotsatira zake, iye adati idzabweretsa ndalama zakunja m'dziko muno ndi mwayi wa ntchito wochuluka.

"Pulojekitiyi ikugwirizana ndi masomphenya a 2063 amene zina mwa ngodya zake ndikufikitsa ulimi pa bizinesi ndi kukuza ntchito za mafakitale.

"Takhala tikungodalira kwambiri ulimi wa nthawi ya mvula chonsecho tili ndi madzi ochuluka amene tikhoza kumagwiritsa ntchito kuthirira mbewu kwa chaka chonse choncho ntchitoyi ikulondolera kumeneko," iye adatero.

Mkulu woyendetsa ntchito ya zomangamanga za pulojekitiyi Martin Chizalema adati pakadalipano magawo 20 mwa 100 a ntchitoyo atheka.

Iye adati chiyembekezo n'choti pofika m'chaka cha 2024 gawo loyamba la ntchitoyi likhala litatha.

"Pali ndondomeko yoti alimi a m'chigawo chimenechi adzayambe kugwiritsa ntchito madzi m'chaka chimenechi kuthirira mbewu zawo kwinako tikumalizitsa," iye adatero.

Boma lidakhazikitsa pulojekiti ya SVTP ndi cholinga chochulukitsa zokolola komanso kukweza ulimi kufika pa bizinesi.

Pulojekitiyi ili ndi mahekitala 43 370 ndipo ndi ya ndalama zokwana US$ 222.7 miliyoni.■



ZITHUNZI: ABEL IKILONI, MANA

Chilima kuyendera pulojekitiyi




Kodi mukudziwa kuti ulimi wa njuchi ndi wosavuta kupanga kaamba koti sulira malo aakulu, komanso sulowa zambiri? Kodi mukudziwa kuti mlimi wa njuchi atha kupeza ndalama zoposa K100 000 kapena kuposa apo pa mng'oma umodzi? ■

KALIMALIMA James Kazembe

